

MAU ONENEDWA NDI NYIMBO ZOIMBIDWA PA ZIGAWO ZINA ZA NTHAWI YACHIPEMBEDZO

Mau Onenedwa Pamapeto Pakuwerenga Buku La Masalmo

Onse: Akhale ndi malemekezo; Mulungu Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera; monga kunali poyamba; kunthawi zatsopano ndi kunthawi zanthawi. Ame!

Dziwani izi: Otsogolera kuwerenga amawerenga vesi ina ndipo mpingo onse umawerenga yotsatira yake. Zimayenera kutero mpakana kumapeto kwa ndime yowerengedwayo. Koma vesi yomalizira imawerengedwa ndi anthu onse: otsogolera kuwerenga ndi mpingo onse.

Mau Onenedwa Pamapeto Pakuwerenga Buku La Chipangano Chakale

Owerenga: Ame!

Onse: Ame!

Mau Onenedwa Pamapeto Pakuwerenga Buku La Chipangano Chatsopano

Owerenga: Ame!

Onse: Ame!

Mau Onenedwa Pamapeto Pakuwerenga Buku La Chipangano Chatsopano (Uthenga Wabwino)

Owerenga: Ambuye adalitse kuwerenga kwa mawu ake onsewa...

Onse: Ndipo kwa iye kukhale ulemerero, ndi chitamandiro. Ame!

Nyimbo Yoimbidwa Pamapeto Pa Ulaliki

(Anthu onse aime)

Onse: Mulungu akhale nao; Ulemerero ndi dalitso; Ndiye Atate, Mwana; Mzimu Woyera, Mulungu m'modzi. Tsopano, poyamba paja; Masiku onse alinkudza; Mphamvu, ulemerero; Dalitso, chipambano. Ame!

Nyimbo Yoimbidwa Pamapeto Pa Zopereka

(Anthu onse aime)

Onse: Ambuye mwini zonsezi, Ulemu tiperekadi; Chikondi tiwonetsanji? Mwapatsatu. Ame!

Chikhulupiriro

(Anthu onse aime)

Onse: Ndikhulupirira Mulungu Atate wamphamvu zonse, wakulenga zakumwamba ndi zapansi; Ndikhulupirira Yesu Khristu, Mwana wake wobadwa yekha, Ambuye wathu; Amene anapatsidwa ndi Mzimu Woyera, nabadwa ndi Maliya m'namwaliyo; Nasautsidwa kwa Pontio Pilato, napachikidwa pa mtanda, nafa, naikidwa m'manda, natsikira kwa akufa; Tsiku lachitatu anaukansa kwa akufa, nakwera kumwamba, nakhala padzanja lamanja la Mulungu Atate wamphamvu zonse; Kudzera komweko, adzadza, kudzaweruzwa anthu amoyo ndi akufa; Ndikhulupirira Mzimu Woyera, mpingo wa Mulungu woyera wa kwa anthu onse, chiyanjano cha oyera mtima, kukhulukidwa kwa machimo, kuukansa kwa thupi, ndi moyo wosatha. Ame!

Pemphero La Ambuye

Onse: Atate wathu wakumwamba, dzina lanu liyeretsedwe, Ufumu wanu udze, kufuna kwanu kuchitidwe; Monga kumwamba chomwecho pansu pano; Mutipatse ife lero, chakudya chatu cha lero; Ndipo mutikhulukire ife zochimwa zathu, monga ifenso tiakhulukira amangawa athu; Musatitengere ife kokatiyesa, koma mutipulumutse ife kwa oipayo; Chifukwa wanu, uli Ufumu, ndi mphamvu, ndi ulemerero, wanthawi zonse. Ame!